



Writer: William R. Flowers
Editor: Emily Ann Rickard
Senior Editor: Dr. Art Criscoe
Christ to the World Ministries
rights reserved

Hard Questions About God Series
Episode 7 of 7: Why Does Evil Always
Seem to Win?

Copyright © 2016

All

DIRECTORIAL INFORMATION

CAST OF CHARACTERS:

Thomas: Narrator, a disciple of Jesus (voice of a mature man)
Philip: Disciple of Jesus (voice of a mature man)
Mary: Friend of the disciples (voice of a mature woman)
Jesus: The Son of God (warm voice of a mature man)

WHY DOES EVIL ALWAYS SEEM TO WIN?

Scripture references: John 18; 19; 20

(Music: Theme music begins, then gradually fades to underscoring during comments by Program Host)

Program Host

Takulandirani ku nkhani yathu ya “Nkhani Yeniyeni”

Takhala tikutsatira masewero okhuza mafunso ovuta; lero tiunika mwina funso lovuta pa onse. Tiyezi tiganazire mafunso asanu awa amene amalongosola za mbiri ya munthu: nkondo. Ziwawa. Chitonzoz. Udani. Kupondereza. .

Kuchokera kale, munthu wakhala akuvutika pakati pa amphamvu ndi ofooka; akupha ndi ophedwa; a ulamuliro wopondereza ndi oponderezedwa. Ponseponse tikayang’ana, timaona chitsimikizo cha kulimbana kwa mphamvu kumeneku, kwa pakati pa cholondola ndi cholakwika, chabwino ndi choipa.

Ndipo ngakhale ife timafuna chabwino kuti chipambane ndipo choipa chosiye, m’badwo ulionse umakumana ndi zosiyana ndi izi, ndipo zimabweretsa kulira komanso kufunsa funso lovuta zedi: Ngati Mulungu ali wabwino, ndipo akulamulira, chifukwa chiyani zoipa zimaoneka ngati zikupambana?

Wokondedwa mnzanga, ngati munafunsako funso limeneli, ndili nanu uthenga wabwino: ndi zoona kuti Mulungu akulamulira, zilibe kanthu zimene mumaona

kuthupi, choipa sichidzapambana nthawi zonse. Koma pamene tikufunafuna mayankho a mafunso ovuta amenewa, tikuyenera tivomereze kuti choipa sichinadze ndi Mulungu; ife anthu tinabweretsa. Mulungu samalanda ulamuliro kwa ena; ife timachita choncho. Kotero ngati tikuyenera kupeza yankho logonjetsa choipa, tikuyenera kuzindikira vuto leni leni, ndipo vuto ndi **ife**. Ife, maka maka kuukira kwathu kwa zabwino ndi Mulungu wachikondi ndilo vuto leni leni. Khalani nafe tsopano pamene tikumaliza masewero athu, mafunso ovuta okhuza Mulungu, ndipo tiunika funso lomaliza komanso losautsa:

“Chifukwa chiyani choipa chimaoneka ngati chimapambana?”

(Music: swells to indicate scene change; then fades to soft underscoring)

Notice that scene changes are depicted with music.

Scene One

INSERT: (Sound effects: nighttime; soft breeze; crickets chirping in the background)

Tomasi: (kufotokoza) Dzina langa ndine Tomasi, ndipo ndinali wophunzira wa Yesu. Kwa zaka zitatu ndinamutsatira pamene anayenda m’dziko lonse, kulalikira uthenga wabwino wa ufumu wa Mulungu, nachiza mazana mazana a anthu ku nthenda zosiyana siyana zimene mungaziganizire.

INSERT: (Sound effects: sounds of a softly crackling fire)

Tomasi: (kufotokoza, kumveka kupuma) Koma izi zachitika tisanatenge msewu wopita ku Yerusalemu. (chapansi pansu) Sindinkadziwa nthawi imeneyi kuti nsewu umenewu ukulunjika kuti. Sindikumvetsetsa chimenea chinachitika:

Yesu anali . . . anali munthu wabwino. Anakakhalapobe, ndikanamufunsa funso:

Chifukwa chiyani choipa chapambananso?

INSERT: (Sound effects: we hear a twig snap nearby and the hoot of an owl in the background)

Tomasi: (kudabwa) Ndani . . . ndi ndani? Kuli munthu kodi?

INSERT: (Sound effects: Thomas listens; but we hear only nighttime sounds)

Tomasi: (monong’ona) Mukuyenera kukhululuka. Ndili wosautsika kuchokera . . . kuchokera nthawi imene anamupha Yesu. Tinali pamodzi pamwamba pa mzinda, pamene anabwera pakati pa usiku ndi muni ndi zibonga, namgwira iye, namtenga iye. Petro anayesetsa kulimbana nawo, koma . . .kumapeto tonse tinathawa, tonse khumi ndi awiri. Sindikudziwa kuti anzanga anachita chiyani, koma ine ndinabisala kumapiri pamwamba pa mnzinda, akumvekabe mapazi, ndimaona ngati nanenso andigwira. **(monong’ona)** koma sanabwerenso.

INSERT: (Sound effects: owl hoots again)

Tomasi: Kutacha m’ mawa tsiku lotsatira, wodzadzidwa ndi mantha, ndinachoka komwe ndinabisala, ndipo ndinalowa mu mnzinda, kuopa kuyang’anana ndi munthu wina aliyense – maka maka asilikali – amene anali ponse ponse. Sindinaonepo ulamuliro ukuonetsedwa ndi asilikali motere; paliponse panali aroma, ndipo ena anazungulira ndende kumene ndimaona ngati am’sunga Yesu ngati, mkaidi.

INSERT: (Sound effects: twig snaps nearby again)

Tomasi: (modabwa) Kuli munthu kodi?

INSERT: (Sound effects: Thomas listens, but we hear only nighttime sounds)

Tomasi: (motsitsa) Mwina ndizimitse moto. Koma iai, iai, ndikatero ndikhala pa chiopysezo cha moto olusa. (kudziyankhula yekha) Limba mtima Tomasi! Usalore phokoso la usiku kuti likusokoneze! (kumveka kupuma mwa phuma) Tsopano – ndinali pati? Oh, inde. Yesu analidi mkaidi wawo. Ndinayesetsa kumvetsera zimene zimakambidwa ndi anthu m’ misewu kooma kuonetsetsa kuti asandidziwe, ndipo ndinapeza kuti Yesu anayesedwa kale ndi akulu akulu a chipembedzo, ndipo anaperekedwa kwa Aroma kuti apachikidwe. (mokweza). Apachikidwe! (kuyankhula yekha) Shh! Samala, Tomasi. Samala.

INSERT: (Sound effects: the owl hoots again)

Tomasi: (kunong’ona) Anamutengera kwa wamkulu wa Aroma, amene anakana kumuweruza Yesu namutumiza kwa Mfumu Herodi, amenenso anakana kumuweruza. Nditamva izi, chiyembekezo change chinayamba kuwala. (kuyankhola mokweza pang’ono) Koma pamene asilikali anamubweretsanso Yesu kwa Wamkulu wa Aroma, modabwitsa akulu akulu a chipembedzo – abwino, komanso anthu a Mulungu – analamula kuti Yesu apachikidwe ngati wolakwa.

INSERT: (Sound effects: Thomas pauses; we hear only the sounds of night for a moment)

Tomasi: (monong’ona) Izi ndi zimene anachita. Anamukhoma pamtanda, nampachika Iye. Polowa dzuwa, Yesu anamwalira. Ndinaona ndi maso anga.

Munthu wabwino, wofatsa, amene anachiza anthu ambiri, amene ananena choonadi chikha chokha, naonetsera chikondi kwa wina aliyense, anamenyedwa mwankhanza, kuzunzidwa, naphedwa pamaso pa anthu onse.

INSERT: (Sound effects: Thomas pauses; we hear only the sounds of night for a moment)

Tomasi: Anatsimikiza kuti wamwalira, anatsitsa thupi lake pamtanda, nakulunga mu nsalu, ndikukaika m’manda. Anapita. Wapita, ndipo zinthu zidzizakhalanso chimodzimidzi. (*kuima kaye*) sindikudziwa kuti ndipite kuti, kapena ndichite chiyani. (*kumveka kupuma*) ndipo sindinaone ophunzira ake kwa masiku awiri apitawa kuchokera pamene Yesu anaikidwa m’manda. Mwina abwerela kwa mabanja awo ndi kuntchito zawo zina ndi zina. Kunyumba! Ndibwerela bwanji kunyumba, ngati kuti palibe chimenea chachitika? Zaka zitatu zapitazo, ndinakumana ndi munthu wodabwitsa kwambiri, wachifundo amene sindinam’dziwepo, ndipo pano, wapiti. Choipa chapambana.

INSERT: (Sound effects: twigs snap again; this time it is obvious the noise was created by footsteps)

Tomasi: (kulira ndi mantha) Ndani . . . ndani ali kumeneko? Ndili ndi mpeni, ndipo ndikutsimikiza, ndikhoza ku . . .

Filipo: (mongong’ona) Shh! Tomasi! Usakweze mawu! Ndine, Filipo!

Tomasi: (ndi mantha) Filipo?

Filipo: (monong’ona) Inde, ndine; ndakhala ndikukuyang’ana ponse ponse.

Zimitsa motoyo, tiye tichoke pano, wina asanakuone.

Tomasi: Wakhala ukundiayang’ana? Tikupita kuti?

Filipo: Kukakumana ndi anzathu.

Tomasi: Ophunzira ena?

Filipo: Inde.

Tomasi: Koma . . . chifukwa chiyani? Kodi zimenezi sizipangitsa kuti atigwire mosavuta?

Filipo: Kuli nkhani. Tsopano, fulumula, Tomasi.

Tomasi: Nkhani? Nkhani yanji?

Filipo: Palibe nthawi yoti ndifotokoze. Zimitsa motowo ndipo nditsatire.

Tomasi: Chabwino. Ndidikire pang’ono.

INSERT: (Sound effects: sounds of shuffling feet, soft thuds as Thomas dumps handfuls of dirt on the fire; crackling dies, replaced by sizzling as fire dies)

(Music: swells to indicate scene change; then fades to soft underscoring)

INTERMISSION

Muwulutsi wa Pologalamu: Zikomo chifukwa chokhala nafe. Mukumvetsera sewero la “Nkhani Mkati mwa Nkhani.” Lero tikumaliza sewero la, “Mafunso ovuta okhuza Mulungu,” yomwe ikuchokera mu zochitika komanso nkhani za anthu opezeka m’Mawu a Mulungu. M’buyomu, m’nkani yathu, yesu, mphunzitsi wodabwitsa, wochiritsa, anagwidwa napachikidwa, ndipo ophunzira ake amwazikana. Opanda mtsogoleri wao, akuopa ndipo akuyembekeza kuti

nthawi ili yonse amene amupha Yesu, awatsatiranso iwo. Masiku awiri adutsa kuchokera tsiku limene Yesu anayikidwa m’manda, pamene Tomasi, m’modzi wa ophunzira, wakumananso ndi wophunzira mnzake, Filipino. Khalani nafe tsopano, pamene tikumaliza komanso kuyankha funso lovuta kwambiri: Ngati Mulungu ali wabwino, kodi chifukwa chiyani choipa chimaoneka ngati chimapambana nthawi zonse?

(Music: underscoring fades out as sound effects return)

Scene Three

INSERT: (Sound effects: nighttime – soft whispering in the background; crickets chirping and a dog barking occasionally)

Tomasi: (kunong’ona) Filipino . . . kodi malo ano ndi ati?

Filipo: (monong’ona) Ndi chipinda chobwereka, cha mnzake wa Yohane.

Ndikhulupilira kuti ndife otetezedwa . . .tsopano.

Tomasi: (monon’gona) Tsopano: ndifotokozere nkhani imene uli nayo ija

Filipo: (monon’gona) Kwatsala nthawi yaitali bwanji kufikira kucha?

Tomasi: (modabwa, monon’gona) Chiyani?

Filipo:(monon’gona) Kucha; nthawi imene yatsala kufikira kucha?

Tomasi: (monon’gona) Chabwino . . . ndione kaye; pamene timalowa

m’nzinda inali ola lachinayi . . . dzuwa lituluka nthawi iliyonse tsopano.

Filipo: (monon’gona) Inde! Inenso ndikuona choncho. Kutanthauza kuti akuyenera kufika pompano.

Tomasi: (monon’gona) Bwera, Filipo; ukunena ndani? Ndipo akuyenera kukhala pati?

Filipo: Maria Magdalena, Mai a Yakobo, ndi Yowana. Apita kumanda.

Tomasi:(Mokweza mawu) Chiyani? Azungulira mitu?

Filipo: (monon’gona) Shh! Usakweze mawu, Tomasi!

INSERT: (Sound effects: whispering in the background suddenly stops; all that we hear for a moment are the sounds of crickets and a barking dog)

Tomasi: (monon’gona) Pepa. Koma chifukwa chiyani anapita kumanda?

INSERT: (Sound effects: the whispering resumes)

Filipo: (monon’gona) Kuti akamalize kuthira mafuta thupi lake. Tinawauza kuti asapite, koma anakakamira.

Tomasi: (monon’gona) Koma iyi ndi misala! Manda anatsekedwa ndipo asilikali achiroma akulondera.

Filipo: (monon’gona) Ndikudziwa . . .

Tomasi: (monon’gona) Ndipo ngakhale atawazemba asilikaliwo, akachotsa bwanji chimwala chimenea chatseka manda aja?

Filipo: (monon’gona)Ndikuvomereza, Tomasi; zoonza zake ndizakuti, tinagwirizana. Koma azimayi sanafune kutimvera. Anati, kutengera zonse zimene Yesu anatichitira, zochepa zimene angachite ndizo kuonetsetsa kuti waikidwa m’manda moyenerera. Ndichithandizo chatu kapena popanda chithandizo chatu.

Tomasi: (monon’gona)Ndiye akufuna aphedwe poyesera! Kapena agwidwe ndi asilikali, amenyedwe, azunzidwe, kenako aulule kumene ife tabisala, kuti aphe tonse! Ndiye chifukwa chiyani tikudikira pano? (mokweza) izi sizoonna!

Filipo: (monon’gona)Shh!

INSERT: (Sound effects: whispering in the background suddenly stops; all that we hear for a moment are sounds of crickets and the barking dog; after a moment a rooster crows in the distant background)

Tomasi: (monon’gona)Dzuwa latuluka. Tikuyenera kuchoka pano, Filipo, Tsopano.

Filipo: (monon’gona)Tichoka, koma tikudikira azimayi kuti abwerere.

Tomasi: (monon’gona)Koma . . .

Filipo: (monon’gona)Sitingachoke popanda iwo, Tomasi.

INSERT: (Sound effects: they pause for a moment; sounds of crickets fades, birds begin to chirp; we hear the rooster crow again, and then the whispering in the background quietly resumes)

Tomasi: (Kupuma, kenako kunong’ona) Ndikuona kuti tisatero...koma abwerera nthawi yanji? Poganzira kuti sanaphedwe kapena kugwidwa.

Filipo: (monon’gona): Anati ngati zonse zitayende bwino, ziwatengera maola awiri kapena atatu. Tsopano dzuwa likutuluka, akuyenera kuona mandawo komanso kupanga chiganizo kuti apitilize bwanji

Tomasi: (monon’gona): Chabwino...zomwe tingachite ndikuyembekeza kuti abwerere pakatha maola awiri kapena atatu? Ndiye pakadali pano tingokhala nkumadikira?

Filipo: (monon'gona) Ndikuona choncho...

INSERT: (Sound effects: a sudden, though not loud, 3 taps, pause, and 1 more tap at the door; all whispering stops and we hear only the birds chirping)

Tomasi: (monon'gona) Akuyenera kukhala Aroma! Awapha azimayi aja, ndipo akubwera kudzatigwira!

Filipo: (monon'gona) Ai ai; awa ndi malo athu achinsinsi! Akuyenera kukhala mnzathu!

Tomasi: (monon'gona) Kapena Aroma ena auzidwa komwe tili ndi azimayi aja asanapedwe! Usayankhe!

Filipo: (mokweza pang'ono) Tsegula chitseko!

INSERT: (Sound effects: soft footsteps, followed by the sound of a latch; door opens; footsteps shuffle in quickly; door closes again)

Filipo: Maria! Chifukwa chiyani wabwera nsanga?

Maria: “*Ndawaona Ambuye!*” (Yohane 20:18)

INSERT: (Sound effects: murmuring rises from all of the disciples trying to speak at once)

Tomasi: Chiyani? Unalowa mkati?

Filipo: Aroma anatsegula manda ndikukulolani kuti muone thupi?

Maria: Ai, ai! Tamuona Yesu, wamoyo! Ndinayankhula naye, ndi . . .

INSERT: (Sound effects: murmuring increases, nearly frenzied)

Tomasi: Unayankhula naye!

Filipo: (Mokweza) Chete! Tamusiye Maria alankhule!

INSERT: (Sound effects: murmuring slowly dies out)

Filipo: (Motsitsa) Ukutanthauza chiyani, Maria, kut...wayankhula naye?

Maria: Titafika, Aroma anali atapita, ndipo chimwala chinali chitachotsedwa. Ndinasuzumira m' manda, ndipo munali anthu awiri, atavala zoyera, ataakhala pomwe panaikidwa thupi.

INSERT: (Sound effects: murmuring springs back to life)

Filipo: (Mokweza) Akulu akulu . . . muloleni amalize!

INSERT: (Sound effects: murmuring slowly dies out)

Maria: Anandifunsa, “*Mzimayi, ukulira chiyani?*” Ndinati, “*Amutenga mbuye wanga, ndipo sindikudziwa kumene amuika.*” (Yohane 20:13)

Tomasi: Wina waba thupi la Yesu!

Maria: Iai! Nditatembenuka, ndinaona munthu wina ataima panja pa manda, ndipo anandifunsa funso: “*Mzimayi, ukulira chiyani?*” (Yohane 20:15) ndipo anatchula dzina langa.

Filipo: (modabwa) Anakudziwa? Koma . . .

Maria: Anati, “*Maria*” (Yohane 20:16). Nditamva dzina langa, maso anga anatseguka. (mokweza). Anai Yesu! Wauka kwa akufa, ndiwamoyo!

INSERT: (Sound effects: murmuring roars back to life as everyone is talking and shouting at once)

(Music: underscoring fades out as sound effects return)

Scene Four

INSERT: (Sound effects: daytime; birds singing in the background, and a soft breeze)

Tomasi: (*kufotokoza*) Patatha masiku asanu ndi awiri. Petro ndi Yohane anabwerera kumanda, ndipo anatsimikiza kuti thupi lake kunalibe. Filipino ndi ena onse anakhulupilira nkhani imene azimayi anatiuza, koma ine sindinakhulupilire. (*kupumira*) Yesu anafa, ndipo palibe chimenea chitasinthe. Chabwino chagonjetsedwa ndipo choipa chapambana. Ndinachoka mu nzinda, ndipo ndinakhala sabata imodzi ndi banja langa, kuyesetsa kuiwala kuti ndinakumanapo ndi yesu. (*kumveka kupuma*) Koma Filipino anandipenzanso, nandiuza kuti ndibwererenso ku Yerusalemu. Anandilonjeza kuti ndikadabwitsika ndipo sindikakhumudwa.

Filipo: Ubwera, Tomasi?

Tomasi: Ndikuona ngati ndibwera. Tithane nazo izi.

INSERT: (Sound effects: Thomas rises to his feet, and we can hear them climbing a set of steps; door opens and closes; we are now inside; daytime sounds suddenly diminish into the background)

Tomasi: Ukudziwa, sindikukhulupilira zimenezi, Filipino

Filipo: Ine ndikukhulupilira

Tomasi: Yesu anafa, Filipino, zimene ananena Maria kapena ena onse zilibe kanthu. “*Pokha pokha ndione mabala m’manja mwake ndikuika chala change pomwe anam’khoma ndi misomali, ndikupisa m’bali mwa thupi lake, sindikhulupilira*” (Yohane 20:25)

Filipo: Taona chitseko, Tomasi – kodi ndichokhoma?

Tomasi: Ndichokhoma. Tsopano, izi ndiye chiyani?

Fiipo:(monon’gona) Tembenuka, dzionere wekha

Yesu:(monon’gona) “*Mtendere ukhale ndi inu*” (Yohane 20:26)

Tomasi: (modzidzimuka) Yesu! Mwa...

(Music: underscoring music begins softly)

Yesu: “*Ika chala chako; ona manja anga. Pisa nkono wako m’thiti mwanga.*

Siya kukaikira ndipo khulupilira” (Yohane 20:27)

Tomasi: (mozizidwa) *Ambuye wanga...Mulungu wanga!* (Yohane 20:28)

(Music: underscoring music swells; then begins reprise of Theme music; softly underscoring comments of Program Host during Our Response to God’s Word)

OUR RESPONSE TO GOD’S WORD

Prograam Host

Mnzanga, choipa chimangooneka ngati chapambana. Koma zilibe kanthu zimene maso anu aona kapena zimene mukumva, masautso ndi kupondelezedwa ndi zoipa sizidzakhala muyaya. Ngakhale mu imfa, choipa sichipambana’ chifukwa yesu wauka kwa akufa ndipo tsopano waima wamoyo ku nthawi zonse ngati Mpulumutsi ndi Mznanu! Kwa ife, amene ngati Tomasi tasintha mitima yathu ndi kukhulupilira, Yesu walonjeza kutipatsa moyo wosatha ndi chigonjetso pa uchimo ndi zoipa, ngakhalenso imfa!

Taonani, Mulungu amakukondani inu ndi ine, ndi chikondi chosatha. Koma machimo athu atilekanitsa ife ndi Mulungu. Mulungu woyera ndi wolungama wapanga njira kuti machimo anthu akhululukidwe. Njira yake ndiyo Yesu Khristu, Mawu a Mulungu a moyo ndi nsembe ya mwana wa nkhusa. Yesu anafera machimo athu. Anauka kwa akufa ndipo ndi wamoyo lero. Ali ndi mphamvu yolowa m'miyoyo yathu ndikutikhulukira machimo nabweretsa chipulumutso chosatha.

Kukhululuka kwa machimo ndi moyo wosatha ndi mphatso ya ulere ya Mulungu. Sitimaipeza pogwira ntchito; timailandira ngati Mphatso. Kuti mulandire chikhulukiro ndi moyo wosatha, tikuyenera kusiya machimo athu ndikuika chikhulupiliro chathu mwa Yesu ndikumulandila Iye m'moyo mwathu ngati mbuye ndi mpulumutsi wathu.

Ndipemphera pemphero lalifupi, lapamtima kwa Mulungu. Inu mvetserani pemphero langali, ndipo ndikamaliza kupempherako ndikutsogolerani inuyo kuti nanu mupumphere pemphero lomwelo

Wokondedwa Atate, ndikudziwa kuti ndine wochimwa. Ndikukhulupilira kuti Yesu anafera machimo anga. Ndikukhulupilira kuti anauka kwa akufa ndipo ndi wamoyo lero. Ndasiya machimo anga tsopano. Ndikuika chikhulupiliro change mwa Yesu yekha kuti akhale mpulumutsi komanso andikhululukire. Ndilandila Yesu m'moyo mwanga ngati mbuye ndi mpulumutsi wanga. Kuchokera lero kupitsa m'tsogolo, nditsatira Yesu. Zikomo], Ambuye Yesu, pondikonda komanso kulowa m'mtima mwanga. Amen.

Now pray the prayer aloud after me. We will pray it a portion at a time. Make the prayer your very own to God. Mean it with all your heart as you pray.

Pano bwerezani pempheroli mokweza kutsatira ine. Tizipemphera modukizadukiza. Inu pempherani motsimikiza, molitanthauza pempheroli ndi mtima wanu onse.

Wokondedwa Atate, (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndikudziwa kuti ndine wochimwa(dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndikukhulupilira kuti Yesu anafera machimo anga,(dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndikukhulupilira kuti anauka kwa akufa ndipo ndi wamoyo lero(dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndasiya machimo anga, (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndikuika chikhulupiliro change mwa Yesu yekha ngati mpulumutsi wanga kuti andikhululukire, (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndilandila Yesu m'moyo mwanga ngati mbuye ndi mpulumutsi wanga. (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Kuchokera lero, kupita mtsogolo, ndim'tsatira Yesu. (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Zikomo, Ambuye Yesu, pondikonda komanso kulowa m'moyo mwanga. (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Amen. (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Mwalandilidwa m'banja la Mulungu!

Pamene tidalira Yesu Khristu ngati mpulumutsi wathu ndikutsimikiza

kumutsatira iye ngati mbuye wathu, akufuna ife tikule ngati okhulupilira.

Mawu a Mulungu akuti, *“Koma kulani m'chisomo ndi chizindikiritso cha*

Ambuye wathu ndi mpulumutsi Yesu Khristu.” (2 Petro 3:18)

Njira imodzi yabwino yoti tikule ndiyo kuwerenga Mawu a Mulungu tsiku ndi

tsiku. Kudzera m'Mawu ake, amatitsogolera kakhalidwe.

Timapeza zimene zimamusangalatsa Iye. Timapezanso zoyenera kupewa, ndi

zomwe zikhoza kutiononga.

Kuonjezera kuwerenga Mawu a Mulungu tsiku ndi tsiku, njira ina ndiyo,

kupemphera. Pamene tiwerenga Mawu a Mulungu, amatilankhula. Pamene

tipemphera, timalankhulana ndi Mulungu.

Tikuyenera kuvomereza machimo athu kwa Iye ndikupempha chikhululukiro nthawi zonse. Kudalira Yesu Khristu ngati mpulumitsi ndi Mbuye sizitanthauza kuti sitidzachimwanso. Tikuyenera kukhala osachimwa. Koma pamene tichimwa, timupemphe kuti atikhululukire. Tikuyenera kupempherera chitsogozo tsiku ndi tsiku. Tipempherenso ena. Kuphatikizapo apabanja athu ndi anzathu. Komanso adani athu!

Sizapafupi kumutsatira Yesu. Wokhulupilira amazunzidwa chifukwa chomutsatira Yesu. Tisadabwe pamene ena atinyoza komanso kutizunza chifukwa chokhulupilira Khristu. Yesu anati, “*Ngati anandilondalonda ine, adzakuondani inu...koma izi zonse adzakuchitirani chifukwa cha dzina langa, chifukwa sadziwa windituma ine.*” (Yohane 15:20-21)

Chikondi ndi chikhululukiro zikuyenera kukhala chikhalidwe cha moyo wanu, ngakhale pamene munyozedwa. Sitikumana ndi zokhoma patokha. Mulungu akudziwa za mayesero onse amene tikumana nawo. Mulungu anati, “*Sindidzakusiyani; kapena kukutayani*” (Ahebri 13:15). Chifukwa cha kupezeka kwake m’ moyo mwathu, tikhoza kunena monga m’ mawu ake kuti: “*Nthandizi wanga ndiye Ambuye, sindidzaopa, adzandichitira chiyani munthu?*” (Ahebri 13:6)

Ambuye akudalitseni koposa pamene mukhalila Iye tsiku ndi tsiku.

(Music: Theme music swells dramatically and fades as broadcast ends)